



چیل کھویو (Chichewa)

# NJIRA YOSAMBILA MALINGANA NDI CHIPHUNZITSO CHA (HANFI)



Shaykh-e-Tariqat Amir-e-Ahl-e-Sunnat  
the Founder of Dawat-e-Islami  
Allamah Maulana Abu Bilal

**MUHAMMAD ILYAS**  
Attar Qadiri Razavi رحمۃ اللہ علیہ

غسل کا طریقہ

**Njira Yosambila Malingana Ndi  
Chiphunzitso Cha  
(Imam Hanaf)**

Hazrat'e Allama Moulana Muhammad Ilyas Attar  
Qadiri Razavi *دامت برکاتہم العالیہ*

**Translation Majlis (Dawat-e-Islami)**

Alami Madani Markaz, Faizan-e-Madina, Mahalla Saudagran,  
Old Sabzi Mandi, Baab-ul-Madina, Karachi, Pakistan  
Contact #: +92-21-34921389 to 91  
translation@dawateislami.net

## **Maktaba-tul-Madina**

**UK:** 80-82 Bordesley Green Road, Birmingham, B9 4TA.

Contact #: 07989996380 - 07867860092

Email: uk@dawateislami.net

**USA:** Faizan-e-Madina, P. O. Box 36216, Houston, Tx 77274.

Contact #: +713-459-1581, 832-618-5101

**INDIA:** 19/20 Muhammad Ali Road, Opposite Mandvi Post Office  
Mumbai - 400 003.

Contact #: +91-022-23454429

**BANGLADESH:** K.M Bhovan, 1<sup>st</sup> Floor, 11, Andar Killa Chittagong.

**HONG KONG:** Faizan-e-Madina, M/F-75, Ho Pui Street, Tsuen  
Wan N.T.

Contact #: +85-98750884 - 31451557

**SOUTH AFRICA:** 61A, Mint Road, Fordsburg, Johannesburg.

Contact #: 011-838 9099

**KENYA:** Kanz-ul-Iman, Near Al-Farooq Hospital, Tonoka Area  
Mvita, Mombasa.

Contact #: +254-721-521916

**TORONTO CANADA:** 1060 Britannia Road Unit 20, 21 Mississauga  
ONT Canada.

Contact #: +141-664-82261

**MOZAMBIQUE:** Mesquita Faizan-e-Madina Rua Alfredo Lawley,  
Esturro, Beira.

Contact #: 00258-848554888 - 00258-822808580

أَلْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

## Pemphero lowerengela bukhu (Du'a)

Werengani *Duwa* ili mmusimu musanawerenge buku lina lilonse la chipembezo kapena poyamba phunziro lililonse la chisilamu, m'chifuniro cha Allah muzakumbukira zonse zomwe mwawerenga  
(إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ)

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَأَنْشُرْ  
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

### Tanthauzo:

Oh Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo akuzindikira komanso nzeru, ndipo mutichitire chifundo Oh! Inu olemkezeka ndi apamwambamwamba.

*(Al-Mustatraf, vol. 1, pp. 40 Dar-ul-Fikr, Beirut)*

**Zofunika:** Werengani Durud Sharif (Swalawat) kamodzi poyamba komanso pomaliza kuwerenga Duwayi.

# Table of Contents

|  |     |
|--|-----|
| <b>Njira Yosambila Malingana Ndi Chiphunzitso Cha (Imam Hanaf)</b> |     |
| Maktaba-tul-Madina .....   | ii  |
| Pemphero lowerengela bukhu (Du'a).....                             | iii |
| Kufunika kwa Durud Sharif ( <i>Swalawat</i> ) .....                | 1   |
| Chilango chodabwitsa!.....   | 1   |
| Ndondomeko ya masambidwe .....                                     | 2   |
| Malamulo atatu okakamizidwa posamba.....                           | 4   |
| Kuchukucha mkamwa .....  | 4   |
| Kusuka mphuno ndi madzi.....                                       | 5   |
| Kusamba kwa thupi lonse .....                                      | 5   |
| Machenjezo makumi awiri (20) kwa mamuna ndi mkazi yosamba....      | 6   |
| Zinthu zisanu m'chimodzi zofunika kusamala a Azimayi.....          | 8   |
| Bala lomanga .....   | 9   |
| Kusamaba kuzakhala Malamulo ngati zinthu zisanu zili mmusizi ...   | 10  |
| Zofunika kutsata pomwe mayi wachira mtenda oyembekezera .....      | 10  |
| Malamulo Asanu .....   | 11  |
| Zoyipa za Kuseweretsa Maliseche (kukhuchumula) .....               | 12  |
| Kusamba madzi oyenda.....  | 14  |
| Ndi nthawi it yomwe ili Sunnah po samba? .....                     | 16  |
| Kodi nthawi it yomwe ziri za bwino kwambiri kusamba .....          | 16  |

|  |    |
|--|----|
| Zolinga zambiri mukusamba umopdzi .....                      | 18 |
| Kusamba Pa mvula.....  | 18 |
| Zimakhala bwanji kwa munthu yemwe wav ala chovala .....      | 19 |
| Samalani posamba muli maliseche .....                        | 19 |
| Ngati kusamba kukuyambisa kuzizira, ndi kutani?.....         | 19 |
| Samalani pamene mukugwiritsa ntchito Bigiri .....            | 20 |
| Mangongo.....  | 20 |
| Malamulo khumi owerengera kapena kugwira Qur'an molingana .. | 20 |
| Kugwira mabukhu achipembezo popanda wudhu .....              | 23 |
| Kuwerenga Durud sharif munthawi yomwe muli odetsedwa .....   | 23 |
| Ngati chala chaviikidwa mu inki.....                         | 24 |
| Kasanjidwe ka mabukhu.....                                   | 25 |
| Kugwiritsa ntchito mapepala posanjikizapo zinthu .....       | 25 |
| Chithunzi cha pa Kabah .....                                 | 26 |
| Chiyambi cha mizimu yoyipa (kusokonezeka bongo).....         | 26 |
| Tayammum (kusamba, kapena kuchita wudhu ndi mchenga) .....   | 26 |
| Ziphunzitso za Mtumiki Patayammamu (Sunna) .....             | 27 |
| Njira za tayammam malingana ndi (Hanafi).....                | 27 |
| Njira makumo awiri ndi zisanu za madani pokhuzana ndi .....  | 29 |
| Maganizo a madani .....                                      | 34 |

أَلْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ  
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

## Njira Yosambila Malingana Ndi Chiphunzitso Cha (Imam Hanaf)

Chonde werengani bukhuli mpaka pamapeto, potelo muzindikira mwina ndi mwina momwe mumalakwa pa nthawi yasomba.

### Kufunika kwa Durud Sharif (*Swalawat*)

Mtumiki wolemekezeka, chikhazikiko cha mitima yathu, wachisoni komanso wachifundo (*Mtendere ndi madalitso a Allah apite kwaiye*) adati: “Werengani *Swalawat* mowirikiza pa ine, mosakaika ndi chiyetso chanu.” (*Musnad-e-Abi Ya’la vol 5, P.458, Hadith 6383, Dar-ul-Kutubul-iimiyat, Beirut*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ تَعَالَى عَلَى مُحَمَّدٍ

### Chilango chodabwitsa!

Sayyiduna Junaid Baghdad عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْهَاتِي (*Chisoni cha Allah chikhale pa iye*) akunena kuti mwana wa Kuraybi عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي (*Chisoni cha Allah chikhale pa iye*) anati, “Usiku wina ndinaziloteri ndipo ndidaganiza zokasamba. Koma poti kumazizila kwambili, mtima wanga udaganiza mwa ulesi nuti ‘utsiku udakalipo wawutali

choti ndifulumilire kukasamba ndichiyani? Ukhoza kusamba m’bandakucha”. Mwachangu ndinalumbira zowupatsa chilango mtima wanga pokasamba ndikuvala zovala nthawi yomweyo ndikusiya kuti zovalazo ziwumile pathupi. Ndipo ndidatelodi. Ndithundithu mtima wonyinyilika pofuna kutsatila malamulo a Allah uyenela kulangidwa munjira ngati iyi. Okondwe abale mchipembezo, mwaona mmene akulu athu akale mmene amavomerezera kunva kupweteka pothana ndi zilakolako zoyipa. Ndithudi khani talongosolayi ili ndi chiphunzitso chachikulu kwa wonse womwe chifukwa cha kudziloter a amalephela kukachita mapephero a Fajr (Subh) kapena kudutsidwa Salaah chifukwa cha ulesi kapena manyazi ndi abale (posafuna kukasamba) kuyiwala kunyazitsidwa kwakukulu kwa m’ moyo womwe ukudza. Pamene kusamba kwakhala kokamiza (*Fardh*), nthawi yomweyo munthu uyenera kutero. Hadith ina ikulongosola kuti, “Angelo salowa m’nyumba momwe muli zithuzi, galu kapena munthu yemwe ali ndi *Janaba*” (*Sunan Abi Dawud, Vol-1, p.109*)

## **Ndondomeko ya masambidwe**

Pangani chitsimikizo (niyah) chomwe chili mmusimu mumtima mwanu mopanda liwu palilime lanu kuti “ndikusamba ndi cholinga choziyera (Taharah)” choyamba, sambani mmanja mpakana nzigong’o katatu. Sambani ziwalo zochotsera zonyasa, ngati muli moyera kapena ayi. tsopano ngati pali mbali ya thupi yomwe yatsalira kuda chotsani nthawi



yomweyo,ndipo pangani udhu monga momwe muchitira musanapemphere. posamba musayiwale kutawasa, komanso kuchapa mapazi. Sopano nyowesani thupi lonse (kusamba) ndi dzanja lanu maka mu nthawi yotentha (munthawi iyi sopo angafunike) zithilenino madzi katatu kuphewa laku manja, katatu ku kumanzere, sunthani malo omwe mukusambila ndikuchapa phazi ngati musatero nthawi yomwe mumapanga wudhu.Musayang'ane Qibla nthawi yosamba zikhuleni thupi lonse ndi manja anu.

Musambe malo omwe muthu sangakuoneni (obisika). Ngati malo amenewa sapezeka munthu ayenera kufunda nsalu yokhutala kuchokera pa mchombo mpakana ku maondo, ndipo ngati nsalu yo khutala palibe aphantikize nsalu zopyapyala ziwili kapena kuposera apo ndipo zingagwire thupi, mabondo akhoza kukhala kunja. (Allah **عَزَّوَجَلَّ** waletsa). Azimayi akuyenera kusamala kwambiri. panthawi yosamba sayenera kuyankhula ngakhale kuwerenga Qur'an kapena duwa ina iliyonse monveka mawu. pokutha kusamba zipuke ndi chozipukutila mwanthawi yomweyo akatha kusamba, ndizabwino kupemphera marakah awiri ngati nthawiyo ikukulolani.

(Book loziwika bwino la Hanafi)

صَلَّى اللّٰهُ تَعَالَى عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

## Malamulo atatu okakamizidwa posamba

1. Kuchukucha mkamwa
2. Kuyika madzi mphuno
3. Kusamba thupi lonse. (*Fatawa-e-Alamgiri, Vol-1-13*)

### Kuchukucha mkamwa

Ziwani kuti kuyika mazi ochepa mkamwa ndikulavula mwanthawi yomweyo sikokwanila. Ndizofunika madzi afike pachiwalo chanu chilichonse cha mkamwa kuchoka pa lilime ndikubwelera ku mmero. (*Khulasatul-Fatawa vol-1, P 21*)

Mazi akuyenera kufika mziwalo zonse za mkamwa mpakana kutseri kwa zino lomaliza, mmipata monse mwa mano ndi mizu, ya mano, mbari zones za lilime mpakana malire a mmelo. (*Durr-e-mukhtar ma'Rad-du-muhtar, vol1, p- 254*)

Ngati musali pa changu, tsukani kummero. Ngati mwatsalira timinofuta nyama, misere ya mtedza, ndizina ndi zina, chosani nsanga. Ngati kuchosa kukhoza kukupwetekani, mukhoza osachotsa. (*Fatawa-e-Razaviyyah, Vol-1P-441, Raza foundation*)

Phunziro losamba ndi kuchosa zotsalira mmano. Zidari zitaphatilira mmano atasamba ndipo iye sanalabade kenako adapephera (salah) popanda kuchotsa zotsalira za mmano, kenako adakumbukira kuzichotsa ndikuchukucha mkamwamo, ndikupemphera. Ndipo pepheroli lidali lovomelezeka. (*Derivred from Fatawa-e-Razayyah, Vol-1, P-2006*)

Ngati dzino logwedera lalimbisidwa ndi zina kapena waya ndiye madzi sakufika, zilibe kanthu.

Kuchukucha mkamwa nthawi yosamba ndi lamulo, ndipo katatu ndi chiphunzitso cha mtumiki (Sunnah)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ تَعَالَى عَلَى مُحَمَّدٍ

### Kusuka mphuno ndi madzi

Kungoyika madzi pang'ono mphuno imodzi, sikokwanila, ndizofunika kutsuka mphuno mpakana kumapeto kuli kafupa kofewa monga mpakana kwayambila fupa lolimba. (*Khulasa-tul-Fatawa, Vo-1P21*) Izi zingachitike poyika madzi mmwamba mwa phuno koma kumbukirani, ngakhale katsitsi kamodzi katasalira mphuno popanda madzi, kusambako sikukukwanila Ngati zimphonongolo zouma zatsalira mphuno ndilamulo kuzichotsa. (*Fatawa-e-Alumgiri, Vol1P-13*) Ndizokakamizidwanso kutsuka ucheya wa mphuno. (*Buhar-e-Sari'at Part 2, p, 34 Madinatul Murshid, Bareilly Sharif*)

### Kusamba kwa thupi lonse

Ndi lamulo kusambisa chiwalo china chili chonse cha pa thupi mpakana pansu (ngakhale tsitsi la malo obisika) maka kuchokera tsitsi la mmutu mpakana zilonda za mmapazi. Pali ziwalo zina, ngati simusala zikhoza osafika madzi, zikatero ndiye kuti kusambako sikukukwanila. (*Fatawa-e-Alamgiri, VI, P14*)

## **Machenjezo makumi awiri (20) kwa mamuna ndi mkazi nthawi yosamba**

1. Ngati tsitsi la mamuna liri lopota, ndi zokakamizidwa kutsuka tsitsi loteleri kuyambira kuchiyambi kwake mpaka komwe lili losapotako (kusonga). Azimayi akuyenera kuli tsuka kumayambiliro ake (atsitsi) ndipo sizofunika kwayiwo kumasula, tsitsi lawo. Komabe ngati tsitsilo lamangika moti sangafike kuchiyambi kwa tsitsi, ndibwino kungolimasula.  
*(Fatawa-e-Alamgir, Vol-1, P.13)*
2. Ngati mauna amphuno kapena makutu Sali otseka ndi lamulo kufikitsamo madzi, pochita udhu ndizofunka madzi. kuzera mphuno, koma posamba ndibwino kufikitsa mauna onse a mphuno ndi mmakutu.
3. Tsitsi lilonse la nzikope, ucheya ndi tsitsi la ku nkhwapa litsambitsidwe kuchokela pomwe la yambila ndi khungu lomwe lifike madzi.
4. Tsukani ziwalo zonse za makutu ndi khomo lakhutu lomwe.
5. Sunthani tsitsi la kuseli kwa khutu ndi cholinga chokuti mutsuke bwino makutu anu.
6. Malire amkati mwakhosi ndi mmelo, sangalowe madzi pokhapokha mutayang'anitsa mutu mmwamba.

7. Kwezani manja mmwamba ndi cholinga choti mutsuke ku nkhwapa bwino.
8. Tsukani mbali zonse za mikono.
9. Tsambani mbali zones za kumbuyo.
10. Welemukani ndi kukweza makwinya a mimba ndi cholinga choti madzi afike pa mimba bwino bwino.
11. Thirani madzi pa mchombo ngati mukukayikila kuti mwina madzi sadafike, ndipo tsukanipo bwinobwino.
12. Tsukani thupi lonse kuchokera pachiyambi mpaka pa mapeto.
13. Tsambitsani makwinya amimba yanu pakati pa mimba mpakana cha mu mchombo.
14. Ngati mukusamba chikhalire musaiwale kusambita mapote (makwinya apakati pa mimba ndi cha mumchombo) apakti pa ntchafu ndi kuseri kwa bondo.
15. Tsukani monse momwe matako akumanila maka ngati mukusamba chiimire.
16. Thirani madzi mbali zonse za ntchafu.
17. Thirani madzi mbali zones za kuseri kwa maondo.

18. Thirani madzi pansi pa umaliseche wa chimuna (chokozero) mpakana ku mabatire ndikumapeto.
19. Thirani madzi pansipansi pa maliseche.
20. Munthu osavinidwa (wamamuna), ngati angakwanitse, akoke mmwamba chikopa cha umaliseche wache ndikuthirako madzi kenako ndi kuchapa umaliseche wachewo mbwino bwino.

### **Zinthu zisanu m'chimodzi zofunika kusamala a Azimayi**

1. Kokerani m'mwamba mabele okugwa ndi kuthila madzi kuseli i kwake.
2. Tsukani malire a mimba ndi momwe mabele akumanilana.
3. Tsukani mbari zonse za kunja kwa umaliseche wanu (pansi ndi pa mwamba pomwe).
4. Nzabwino kwambiri kupisa ndi chala kumaliseche ndi kutsukako, koma sizokakamizidwa.
5. Ngati mzimayi ali kumwezi panthawi yo samba, ndi zabwino kwambiri kutsuka ku maliseche ndi sanza za nsalu komanso ndi zoumilira za magazi kumaliseche kwake.

## Bala lomanga

Bandechi ngati ya mangidwa pa bala lonse ndipo ndi zovuta kumasula, kapena kumasulako kungabweletse vuto, mukhoza kungopukuta pa mwamba pa bandechilo (sanza) ndizokwanila, chimodzimodzi ngati chiwalo, chayandikila bala, kutsuka chingabweretse vuto, mukhozanso kungochipukuta ndi madzi ndi zokwanilanso. Bandechilo (sanza la pa bala) lisamangidwe malo omwe Sali opereka chiopyezo ndi bala, kapena pena pali ponse posakhuzana ndi bala ndibwino kumasula, apo ayi ndiye kuti kusamba sikukukwanila.

Ngati ndi zotheka kumanga bandechi (sanza la pa bala) kuonjezela malo omwe siovulala, mwachitsanzongati bala liri pa khungu la panja pa chiwalo ngati mkono ndipo bandechi (sanza la pabala) limangidwe pa mkono kuvindikila malo omwe alibe bala, ndiyekuti ndizokakamizidwa kusambisa mbaliyo mutamasula, koma ngati ndi zosatheka ngakhale kumasula bandechiyo ndikotheka, zivuta kubwezeretsa bandechiyo, ndipo izi nzopereka chopysezo ku balalo, ndiyekuti, kungopukuta ndi madzi, nzotheka. ndipo mbali yomwe ndiyosa vula koma ilimkati mwa bandechi, siizalabadilidwanso. (*Hashiya-tul-Tahwi-o-Maraqil falah, P-143*)

صَلَّى اللّٰهُ تَعَالَى عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

## **Kusamaba kuzakhala Malamulo ngati zinthu zisanu zili mmusizi zachitika**

1. Kutulusa madzi oyambilira omwe amasogozana ndi umuna mwina chifukwa chachilakolako.
2. Chilakolako (kukhumbila mkazi). (*Fatawa-e-'Alamgir, Vol, P-4*)
3. Kuzilotela pogona. (*Khulasa-tul-Fatawa, Vol1, P-13*)
4. Kulowetsamaliseche amamuna kumariseche ankazi, ngakhale, musanameme, kapena kukoza umuna nonse mukuyenela kusamba.
5. Panthawi yomwe muthu wa nkazi wayamba kudwala matenda akumwezi. (*Haid).ibid, P-97*)
6. Mukatha kuchila (kubeleka mwana) (Nifas). (*Tabyun-ul-Haqaiq, (vol-p-17)*)

Azimayi ambiri amaganiza kuti mzimayi akabeleka masiku ake oyembekezera ndi okwana makumi anayi (40) koma izi sizilichoncho chonde welangani mawu otsatila ali mmusiwa.

## **Zofunika kutsata pomwe mayi wachira mtenda oyembekezera (Kubereka)**

Magazi omwe amatuluka mmayi akachila kumene (kubereka) amatchedwa 'nifas' ndipo malire otulukila magazi amenewa ndi



masiku okwana makumi anayi (40) ndipo ngati magaziwa akutulukabe mopitilira masikuwa, ndichisonyezo choti mmayi akuyenela kusamba pakutha kwa masiku okwana makumi anayi) (40) ndipo ngati magazi asiya kutuluka masikuwa asanakwane (40) kapena mphindi imodzi atangochila (kubereka), mayi ameneyu akuyenera kusamba basi, ngati magaziwa asiya kutuluka, ndipo ndikuyamba kupemphera (salah) komanso kusala kudyu, koma ngati magazi ayambilanso nkati mwamasiku makumi anayiwa (40) masikuonsewa kuyambira kochila mpakana kumaliza kutuluka kwa magaziwa kuzatengedwabe ngati 'Nifas' mwachitsanzo kutuluka magazi kwasiya kutha kwa mphindi ziwiri mayi atangobereka kumene ndipo iye mkuyamba kusala ndi kupepmhera pambuyo poti wasamba koma magazi mkuyambila patatha pmhindi ziwir masiku makumi anayi (40) asanakwane, ndiye kuti masiku onsewa makumi anayi (40) azawerengedwa ngati Nifas, kutero ndiye kuti mapemphero (Salah) ndi kusala kudyu (Sawm) zizakhala zopanda ntchito. Ngakhale Ili pemphero lobwenza, kapena Kubwezeretsa kutsala kudyu ndithudi mukuyenera kubwereza zonsezi munthawi iyi. *(Derived from Fatawa-e-Razaviyyah, Vol, 4, P354-356, Raza Foundation)*

## **Malamulo Asanu**

1. Ngati madzi oyambilira a umuna atuluka popanda kumema, mwachosanzo, kungotuluka mwina chifukwa chonyamula chitsulo choremela kapena kugwa kuchokera

- pa mwamba kapena chifukwa cha vuto la mitsempha lobwela munthawi ya chimbudzi, kusamba sikuzakhala kokakamizidwa. (*Maraqil falah ma'Hashiya-tul-Tahtawi p96*)
2. Ngati umuna wasankhika ndi kugwa pansu munthawi yomwe mukukoza kapena munjira ina iliyonse mopanda kumema, Kusamba sikuzakhala kokakamiza, kungoti Udhu wanu uzakhala wutawonongeka. (*Bahar-e-Shar'at, part 2, P-38 maktaba Raviyyah*)
  3. Ngati mwazilotela ndipo mwakumbukira kuti umuna unatuluka koma sunafike pa chovala chanu, Kusamba sikokakamizidwa.
  4. Ngati munamema nthawi ya mapemphero, ndipo mumamva kuyenda kwa madzi osagana ndi umuna, ndipo mwamaliza kupemphera musanatuluse umuna, pempherolo liwerengeredwa, koma kusamba kukhala lamulo. (*Fath-ul-Qadir, Vol-1, P54*)
  5. Kutulutsa madzi anthupi osagana ndi umuna chifukwa choseweretsa umaliseche (kuchikichaa chokozera), Kusamba kuzakhala lamulo komanso ndi tchimo kutero. Ndipo munthu ameneyu amtchedwa Mal'un otembeleledwa.

## Zoyipa za Kuseweretsa Maliseche (kukhuchumula)

Al'la-Hadrat Maulana Shah Ahmad Raza (رحمۃ اللہ تعالیٰ علیہ) anafunsidwa mafunso osatilawa: pali Munthu okhuchumula

chokozeru (Majiluo) yemwe sapewa manyazi ngakhale atalangizidwa; kodi iyeyu azakhala mbali iti pa tsiku ya chiweluzo? chonde tiziwitseni ma duwa omwe angatipewese kukhalidweli”

Ala-Hadrat adayankha” ndiwochimwa, ophwanya lamulo, olakwa pochita tchimo lalikulu, patsiku lachiweluzo, gulu la anthu oterewa azaukitsidwa kwa a kufa ali ndi mimba (wodwala pakati) ndipo azachoititsidwa manyazi pa maso pa magulu la anthu. Izi zikuwadikila ngati iwo safuna kulapa kwa Allah **عَزَّوَجَلَّ** patchimo lawoli. Allah (**عَزَّوَجَلَّ**) amakhululuka kwa amene afuna kuwakhululukira ndipo kulanga amene afuna kuti amulange. Munthu ameneyu awerenge mawu awa” *wala Hawula wala kuwata illah billahi li a lliyi*” mowilikiza, ndipo ngati angakumane ndi mayetsero atsatana kuti achitenso tchimoli (kuchikicha malitseche) iye ayazamile kwa mulungu Allaha (**عَزَّوَجَلَّ**) ndipo anene ndikusimikiza muntima kuti La Hawula, Ndipo azipemphera mapemphero onse asanu (salah) ndipo pa kutha pa pemphero la kummawa aziwerenga cha muntima Surah Ikhras (Kullihu Wallahu Ahdu) mowirikiza. Allah (**عَزَّوَجَلَّ**) ndiye akuziwa bwino” (*Fatawa-e-Razaviyyah, Vol-22*)

Zinalembedwa mu Shajra-e-‘Attariyyah’ kuti ngati wina awerenga Sura Ikhras khumi ndi chimozi (11) mmawa wina uliwonse, satana ndi omusatila ake sazakhala naye pompangisa munthu otereyu kupanga tchimo, pokhapokha yekha atachita tchimo) ngati mukufuna kuziwa zambiri zokhuzana ndi chionongeko choza chifukwa cha kukhuchumula chokozeru

ndi kutulutsa umuna, chonde musanyalanyaze werengani mkabukhu kotchedwa **Amrad Ki Tabahkariyan** lorembedwa ndi Maktabah-tul-Madina)

## **Kusamba madzi oyenda**

Ngati wina akusamba madzi oyenda monga ngati munsinje, kapena madzi oyenda kuchokera pa Damu, ndikukhala mmadzimo mwakanthawi, ndiye kuti Sunnah ya katatukatatu posamba ndi kupanga udhu izakwaniritsidwa. Nzosafunika kuvuula ziwalo mmadzi kokwana katatu. komabe ngati mukusamba mmadzi oti sayenda, ngati damu, ziwalo zukkuyenera kusambisidwa katatukatatu, monga mwa Sunnah. Kuyima pa mvula kapena pampope wa madzi malamulo ake mchimodzimodzi, ndi kusamba ku nsinje.

Mwina mukupanga wudhu mmadzi oti ndi oyenda, chitsanzo nsinje, kungoviika ziwalo kwakanthawi ndi zokwanila. Chimodzimodzi kupanga wudhu madzi oti angoyima, yendesani katatu ziwalo zanu, mokwanila kusambisa ziwalo (katatukatatu).

*(Durr-e-Mukhtar, Rad-dul-Muhtar, Vol-1, P-320)*

Mwazonsezi kusamba, kutsuka mkamwa ndi kutsuka mphuno zikuyenela kuchitika chimodzimodzi.

Malamulo osambila pa madzi a shawa, kapena tinene kuti mpope wa ku bafa, ndi chimodzimodzi ndi kusamba mmadzi omwe ali oyenda (mwachitsanzo mu nsinje)

“Fatawa-e-Ahl-e-Sunnat” (lomwe silinapangidwe pa blishi) lalongosola kuti kusamba pa shawa ndi chimodzimidzi ndikusamba madzi oyenda, izi zikutanthauza kuti ngati wina akusamba shawa, kapena madzi oyenda kapena mwina akupanga wudhu kumene, ndiye kuti Sunnah ya katatukatatu izakwanilisidwa. Buku la Durr-e-Mukhtarr, lidati, ngati wina wayima mmadzi oyenda kuchoka mmwamba, mudamu lalikulu kapena pa mvula mwa kanthawi koti kukukwanila kusamba, ameneyo wakwanilisa Sunnah yonse ya masambidwe ndi wudhu omwe. (*Durr-e-Mukhtar, Rad-Muhtar, vol-1, P 291*)

Kumbukirani! Kusuka mkamwa ndi kusuka mphuno ndikofunikira munthawi yosamba

Samalani ndi zinthu izi pa nthawi yomwe mukusamba pogwiritsa ntchito Shawa

Ngati mukusamba shawa mu bafa, ziwani kuti nkhope yanu ndi kumbuyo simuna yang’anitse ku Qiblah, kutanthauza kuti zonse ziyang’ane pakatikati pa mulingo wa makumi anayi ndi asanu (45) digirizi kuchokera ku Qiblah. Kotero nkofunikira kuti nkhope yanu ndi kumbuyo kwanu simunayang’anise ku mulingo wa makumi anayi ndi asanu (45) digirizi. Anthu ambiri sazindikila izi.

Koyang’anitsa kwa bwino kwa chimbudzi chokumba Chonde yang’anani komwe shawa yayang’ana ndi chimbudzi chokumba mnyumba mwanu monga kagwiritsidwe ntchito ka kampasi

ndi zida zina. Ngati zalakwika, zikonzeni kuti pasiku la chiweluzo mukathe kuzemba zowawa zoza chifukwa cha machismo ang'ono ang'ono ngati amenewa.

Ndiza bwino kupeza w.c.yopangidwayoyikilidwa kale ndi mulingo wa makumi asanu ndi anayi (90) digirizi molingana ndi komwe Kaba ili ngati mwachitsanzo komwe mutu wathu timayang'anisa pambuyo poti pemphero (salah) latha. Anthu alunso la zomangamanga pogwiritsa ntchito miyala ya mtengo wa patali amamanga mwamakono zedi ndipo mokongoletsa nyumba ndipo salabadila ndondomeko zokhuzana ndi Qiblah. Nsilamu aziganizila za bwino za moyo omwe uli nkuza osati za kukongola kwa nyumba izi nzosafunikira kwenikweni.

## **Ndi nthawi it yomwe ili Sunnah po samba?**

Ndi Sunnah kusamba tsiku la chisanu, tsiku la Eid-ul-Fitr, Eidul-ul-Adha, tsiku la Arafa 9<sup>th</sup> Zul-Hajja-tul-Haram) ndi nthawi yomwe mukufuna kuvala Ihram. (*Fatawa-e-'Alamgiri, Vol-1P-16*)

## **Kodi nthawi it yomwe ziri za bwino kwambiri kusamba**

Ndizabwino kwambili kusamba munthawi iyi

1. Pamene muli pa Arafat
2. Pamene muli pa Muzdalifah
3. Pa nthawi yomwe mukupita ku malo odalitsika a Haram

4. Pamene mukuziyandikisa ndi bwalo la milandu la mtumiki wathu Muhammad (Mtendere ndi madalitso zikhale Kwa iye)
5. Pomwe muli pa Tawaf
6. Pomwe mukufika pa Mina
7. Pamene mukulowa mu Shab-Bara'at (pa tsiku la khumu ndi chisanu la mwezi wa Shabani)
8. Pamene mukulowa utsiku olemkezeka wa Layilatul Qadir
9. Utsiku wa pa Arafah
10. Panthawi ya chikumbutso (monga tsiku la Milad Nabee)
11. Misonkhano ya madalitso
12. Pamene mwatha kusambitsa ntembo
13. Munthu amene wachila matenda a Misala
14. Pamene mwayamba kuzindikira
15. Pamene mwachira kuchokera kumankhwala ozunguza bongo
16. Pamene mwalapa Kwa Mulungu
17. Pamene mukuvala chovala cha nyuwani
18. Mukafika kuchokera ku ulendo wa kutali

19. Pamene mwachira matenda otuluka magazi ku maliseche mwina chifukwa chodwala (maka azimayi)
20. Pamene mukufuna kupempherera pa zuwa
21. Pamene mukufuna kupempherera nvula (Salatul-Istisqa)
22. Panthawi yomwe muli ndi mantha, muwutsiku oopysa ndi pomwe pachitika ziphaliwali
23. Pamene thupi ladetsedwa ndi zosaziwika bwino.  
*(Bahar-e-Shariat, part 2P-41)*

## **Zolinga zambiri mukusamba umopdzi**

Ngati zinthu zingapo zachitika, koma mufuna kusamba kamodzi mwachitsanzo, kuziloteri utsiku, komano ndi tsiku la Eidul-Fitr komanso ndi tsiku la Chisanu, ndi zokwanila kusamba kamodzi ndi zolinga zonsezi, ndipo malipilo ake azaperekedwa. *(Durr-e-Mukhtar, Rad-Dul-Muhtar, vol-1P-34)*

## **Kusamba Pa mvula**

Kusamba pomwe mutavala zogwira thupi pa maso pa anthu ena ndi zoletsedwa. *(Fatawa-e-Razaviyyah, Vol-3 p 306)* Nagati mukusamba pa nvula ndithudi zivindikireni shawelo yokhutala bwino mpaka kupitilira malire athilauzala ndi cholinga choti mtundu ntchafu zanu zisaonekele pamene mwavala thilauza yonyowa.



## **Zimakhala bwanji kwa munthu yemwe wav ala chovala chomukwana?**

Ndi zosaloledwa kuona chiwalo cha munthu wina chomwe cha vindikilidwa ndi nsalu yothina kapena chomasuka, koma mwina chothina muziwalo zina chifukwa cha mphepo, kapena chogwira chifukwa chosamba pa mvula, munyanja ndi zina zotero. Munjira ngati izi mapangidwe achiwalo. mwachitsanzo mmene ntchafu yazungulira ikuonekera. Malamulo omwewa akugwiritsiridwanso ntchito poona chiwalo kuzela muzoonekera ngati nsalu chomwe chavindikiridwa ndi munthu yemwe wav ala chovala chogwira thupi.

## **Samalani posamba muli maliseche**

Mwina mukusamba maliseche nokha kapena mwavala thilauza yomwe ikuonetsa ntundu wa ntchafu chifukwa chogwira thupi pomwe ya nyowa, tsimikizani kuti nkhope kapena mbuyo yanu sizina yang'ane ku Kabah.

## **Ngati kusamba kukuyambisa kuzizira, ndi kutani?**

Ngati wina ali ndi matenda onva kuzizira, kapena ali ndi matenda amaso, ndiyeno malingana ndi iyeyo nzonena kuti akasamba kuyambira kumutu matenda amakula, kapena amanva ululu, ndi oloedwa kusamba kuyambira kukhosi kokha, koma asayiwale kutsuka mkamwa ndi kuthira madzi mphuno ndipo apukute mutu wake ndi tsanza lonyowa ndipo kusamba

kuzakhala kokwanila akatero. Koma akachira akuyenera kumasambisa mutu wake bwino bwino kusamba kosalirasalira sikwabino. *(Bahar-e-Shariat 2, p36)*

## **Samalani pamene mukugwiritsa ntchito Bigiri**

Pomwe musamba pogwirisa ntchito bigiri, muyenera kuyikhazika pa mwamba monga pa sutulu, kapena pa mwala ndi cholinga choti dontho za madzi obwerera posamba zisamagweremonso, chimodzimodzi, kapu yomwe mukugwiritsa ntchito posamba musayikhazike pansi.

## **Mangongo**

Ngati muli ndi zingongo mutsitsi mwanu, sizofunikira kwambiri kumacula posamba. *(Bahar-e-Shariat, part2 P-36, Madina-tu-Murshid Bareilly Sharif)*

## **Malamulo khumi owerengera kapena kugwira Qur'an molingana ndi ukhondo**

1. Ngati ukhondo uli vuto kwa munthu ndi zoletsedwa kulowa munzikiti, kuchita Tawaf, kugwira Qur'an, kuwerenga Qur'an popanda kuyigwira, kulemba vesi, kulemba ma Tawizi amu Qur'an (izindi zoletsedwa pamene mukugwira ma pepala ndipo ngati simukugwila palibe vuto) (Fatawa-e-Ahl-e-Sunnat). Chimodzimodzi kugwira ma Tawizi a mu Qur'an, kugwira kapena kuvala chingwe chomwe chiri ndi

ma vesi a mu Qur'an kapena ma Haruf-e-Muqatta'at zomwe za lembedwa nkati mwake, ndi zoletsedwa. (*Durr-e-Mukhtar, Rad-dur-Muhtar, VI, P343*) (Palibe chionongeko china chilichose chingaze chifukwa chovala Tawizi yomwe ya kutilidwa mu pepala la pulasitiki)

2. Ngati Qur'an ili yokutilidwa, palibe vuto kuyigwira popanda wudhu kapena kusamba. (*Al-Hidayah ma'Fath-ul-Qadir, Vol -I, P149*)
3. Chimodzimodzi palibe vuto kugwira Qur'an ndi sanza la mmanja lopukutula thukuta (Handi kachifi) yomwe ikukhuzana ndi chovala chanu, kapena yakutilidwa pa Qur'an. (*kuchokera kwa Rad-dul-Muhtar, Vol-1, P-24*)
4. Ndi zoletsedwa kugwira Qur'an ndi sanza la shati kapena ndi mbali ya mpango wa kumutukapena ndi tawelo yozipukira posamba kumachita kuti mbali inayi ili pamtima izi zili chonchi chifukwa zinthu zimenezi zimatha kukhala ndi litsiro la Janaba. (*Durr-e-Mukhtar, Rad-dull-Muhtar, Vll P537/ Bahar-e-Sharir'at, P42, Madina-tu-Murshid, Bareilly Sharif*)
5. Palibe vuto linalililonse lingaze chifukwa chowerenga vesi ya mu Qur'an ndi cholinga chopanga Duwa kapena pemphero lina lakemonga kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ, kuwerenga اَلْحَمْدُ لِلَّهِ عَزَّوَجَلَّ, monga mo Allah, mwina kuwerenga kumene اِنَّا لِلّٰهِ وَاِنَّا اِلَيْهِ رٰجِعُونَ, munthawi yomwe tanva uthenga wa imfa ya nsilamu zathu kapena ndicholinga chomukweza

Allah (عَزَّوَجَلَّ) kuzera mukuwerenga Sura Fatiha, Ayatul-Kursi mavesi atatu a Surah Hashir, koma ngati kuwerenga ma vesi onsewa mulibe cholinga chowerenga Qur'an. (*Kuchokera kwa Fatawa-e-'Alamgiri, Voll, Pa38*)

6. Makulli atatu akumapeto kwa Qur'an akhoza kuwerenga posiya mawu a Kull ndi cholinga chomutamanda Allah (عَزَّوَجَلَّ). Ngakhale kuwerenga mosaganiza ndi Kull, koma ngati muli odesedwa sizololedwa. ndipo izi zizakhala ngati mukuwerenga Qur'an ndipo cholinga chanu (Niyah) chikhala cha pa chabe. (*Bahar-e-at, part 4, p43 Bareilly Sharif*)
7. Ndi zoletsedwa kugwira Qur'an kapena verse ina iliyonse popanda wudhu. Komabe ndi zololeledwa kuwerenga chamuntima, kapena pomangoyiyang'ana qur'aniyo. (*Rad-dul-Muhatar, Vo1P352-Bahar-e-Shariat part 2, P43, Madina-tul-Murshid Bareilly Sharif*)
8. Ngati wina alibe wudhu kapena sanasambe ndi vuto lake ndipo Sali oloedwa kugwira ziwiyazi za mnyumba zomwe zili ndi ma aya amu Qur'an (mavesi) omwe alongosoledwa mkati mwake. (*Fatawa-e-Razaviyyah, vo, 1P39*)
9. Kugwiritsa ntchito ziwiyazi ndi zosasangalatsa. Komabe sikuti pali chilango kumweramo madzi ndizina zotero. (*Bahar-e-Shari'at, part 2P39*)
10. Malamulo omwewanso akugwila ntchito pogwira kapena kutanthauzila Qur'anmu chiyankhulo cha chi Urudu, Persian kapena muchiyankhulo china chilichonse. (*Fatawa-e-'Alamgiri, Vol-1, P39*)

## **Kugwira mabukhu achipembezo popanda wudhu**

Ndi zinthu zonyasa kugwira (Makruh-e-Tanzihi) kwa munthu yemwe alibe wudhu komanso kusamba ndi kokakamizidwa kwa iye ndi kugwira ma buku ngati a Fiqh (ndondomeko za chipembezo cha chisilamu), Tafsir, (Qur'an yo tanthauzidwa nziyankhulo zina) ndi mabuku a ma Hadith. (*Fatawa-e-'Alamgir, Vol-1, P39*)

komabe mukhoza kugwira ndi nsalu mabukhu oterewa, koma ngati ali ndi ma vesi mkati mwake oti ndi a mu Qur'an, ngakhale ma tanthauzidwe ake, sibwino ndipo ndi zoletsedwa (Haram). (*Bahar-e-Shari'at part 2-43, Madinatul-Murshid Bareilly Sharif*)

Ndi zofunika kusamala, sibwino kuwerenga ma bukhu achisilamu, omwe ali ndi ma vesi amatanthauzo mkati mwake mulibe wudhu

## **Kuwerenga Durud sharif munthawi yomwe muli odetsedwa (Mulibe Tahara)**

1. Palibe cholesa china chilichotse kuwerenga Darud Sharif pomwe musana sambe, koma ndikofunikabe kutsuka mkamwa kapena kupanga kuyamba wudhu kumene
2. Kuyankha Azana ndi kololedwa pa nthawi yomwe simunasambe.

## Ngati chala chaviikidwa mu inki

Chala cha munthu yemwe amaphika, chapakika ufa, kapena mwina munthuyo amalemba ndiye chala chapakika inki ndi madontho ena aliwonse asiyidwa ndi ntchenje khaya uzuzu, zonsezi sizizakhuzana ndi kusamba kwa munthu ngati chovala chanu, kapena chili chonse chakhuzidwa ndi madonthowa chizakhala chilibwinobwino. *(Durr-e-Mukhtar, Rad-du-Muhtar, VI 1P316)*

Komabe ngati mwazindikira zoterezi ndibwino kungozikonza (kuchapapo kapena kuchosa mwina muli monse) komano pepmhero lanu (salah) yomwe munaswali madonthowa alipobe, izakhala yolandilidwa inshaalah. *(Jad-dul-Mumtar, Vol, 1p111)*

Ndi nsinkhu wuti mwana amakhala kuti wakula (kugwa mdothi) Anyamata amaziwika kukula pa nthawi yomwe ayamba kuona zizindikiro ngati kuziloteru maka pakati pa zaka zokwana khumi ndi ziwiri (12) ndi zaka khumi ndi zisanu ndipo atsikana, pamene ayamba kutuluka ukazi (munjila yo kuziloteru) pakati pa zaka zisanu ndi zinayi (9) ndi zaka khumi ndi zisanu. Panthawi yomwe ana atha nsinkhu, ndipomwe amayamba kutsata malamulo Amulungu (shar'ah) ndipo panthawi yomwe ayamba kuziloteru, ndipomwe amakhala odesedwa (opanda Tahara). Koma ziwani kuti ngati palibe zizindikiro za kuziloteru, ndiye kuti zaka zothera nsinkhu ndi khumi ndi zisanu (15) malingana ndi Hijiri Kalenda. *(Al-lubab fiSharh-iKitab, Vol-2, P16)*

## Kasanjidwe ka mabukhu

1. Choyamba bkhu la Qur'an likhale Pamwamba pa mabukhu onse mwachitsanzo Tafsir, Hadith, Fiqh ndi mabukhu ena onse achisilamu akhale motere. (*Durr-e-Mukhtar, Rad-dul-Muhta, Vol1p354*)
2. Musakhazike china chilichonse pa mwamba pa mabukhu achisilamu khaya ndi cholemba chimodzimodzinso musakhazike chinachilichonse mukatundu yemwe mkati mwake muli ma bukhu achipembezo.

## Kugwiritsa ntchito mapepala posanjikizapo zinthu

1. Ndi zoletsedwa kugwiritsa ntchito mapepala a mabukhu azachipembezo. Kugwiritsa ntchito nsalu zoyala pa bedi, nsalu zoyala pa kudy a zomwe za dindidwa zinthu zina kapena kulembedwa (monga zina la kampani) muchiyankulo china chilichonse ndi zoletsedwa. (Kuchokera kwa. (*Durr-e-Mukhata, Rad-ul-Muhtar, Vol1,p355-4356*))
2. Zilembo za ziyankhuilo zonse zigwiritsidwe ntchito. (*Rad-dull-Muhtar, Vol-1, P607*) Ngati mukufuna kuziwa zambiri werengani buku la “Faizan-e-Bisimillah” mu buku la Faizan-Sunnat)
3. Kawirikawiri zina la kampani limatha ku dindidwa pakona pa chopempherela, chonde chotsani, mwanjila ina iliyonse.

## Chithunzi cha pa Kabah

Ngati mugwiritsa ntchito choyala pansi popempphera chomwe chili ndi chithunzi cha Kaba Dome yopatulika yomwe imakhala ya girin, ndizoopsa kwambiri kuponda pachithunzi choterechi, kapena kugwadilapo kumene panthawi yomwe mukupempherera (salah). Chifukwa sizabwino kugwiritsa ntchito zoyala zotere. (*Fatawa-e-Ahle-Sunnat*)

## Chiyambi cha mizimu yoyipa (kusokonezeka bongo)

Mizimu yoyipa kapena kuti kubwebweta (waswaha) zimayamba chifukwa chokozeru ku malo osambila (bafa). Hadrat Sayyiduna Abdullah bin Mughaffal رَضِيَ اللهُ تَعَالَى عَنْهُ adalongosola kuti Mtumiki wa Mulungu (صَلَّى اللهُ تَعَالَى عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ) adaletseratu kukozeru malo osambila ngati ku bafandipo adati, ” palimbe kukayikitsa kwina kuli konse kukoza ku malo osambila kumayambisa matenda obwebweta’ . (*Sunan Abi Dawud Vol.1, P. 44, Hadis 27*)

## Tayammum (kusamba, kapena kuchita wudhu ndi mchenga)

Zokakamizidwa za Tayammam

Njirazi zilipo zitatu (3)

1. Cholinga, kapena kutsimikiza (Niyah)
2. Kupukuta kumaso ndi manja
3. Kupukuta mikono yonse kuphatikizirapo zigongono  
(*Bahar-e-Shari'at, part2, P.65, Madiana-tu-Murshid, Bereilly Shaif*)



## Ziphunzitso za Mtumiki Patayammamu (Sunna)

1. Kuwerenga Bisimillahi
2. Kumenyetsa manja pa bwalo (osati la kapinga ngati la zamasewero)
3. Kuyendesa manja kanayi
4. Maja anu akhale ndi mipata (zala zibalarike)
5. Wombani mmanja koma musapange phokoso
6. Pukutani kumaso choyamba kenako manja
7. Apukuteni manja wonse kamozikamozi mwachangu
8. Pukutani mkono wa manja kamodzi, kenako wa manzere
9. Zinyamuleni ndevu mmwamba (khilal)
10. Nyamulani mmwamba zala kuti muone ngati zafika dothi. Ngati fumbi tsilinafike mwachitsanzo manja anu anamenya pa mwala ndiye fumbi alibe, zikatero ziwani kuti khilal ya manja izakhala yokakamizidwa, chifukwa sikofunikanso kumenyesa manja pa bwalo kawiri. (*Bahar-e-Shari'at, part.2, p.67, Madina-tul-Murshid, Bareilly Sharif*)

## Njira za tayammam malingana ndi (Hanafi)

Pangani niya (cholinga) muntimapopanga Tayammamu (Niya ndi dzina la cholinga chomwe munthu umanena muntima

usanapange chomwe ukufuna kupangocho, ndipo ndibwino kunena molankhula bwinobwino, mwachitsanzo, ndikupanga tayammamu ndicholinga choziyeretsa kuti ndithe kupemphera (sala). Werengani Bismillillahi manja anu ali otambasula ndipo zala zikhale zitabalalika ndipo amenyeseni pa pamalo pomwe mukufuna kupangila tayammamu (monga mwala, mwala wa layimu, njerwa, khoma kapena nthaka ndi zina zotero) ndipo sunthani manja kokwana kanayi ngati manja azaza fumbi lichepeseni posasa mmanaja. Pukutani nkhope yonse ndi manja anu ndipo pasasale pena paliponse, Tayammamu yanu izakhala yopanda ntchito ngati mbali yoyenerera sidafikire fumbi angakhale katsitsi. Menyesaninso manja anu kawiri pomwe mukupangira tayammamu ndipo pukutilani mikono yanu yonse mpaka mzigongono zanu zonse. Njira ya bwino yochitira izi, Choyamba pukutani dzanja la manja ndi mkati mwa zala zinayi za mkono wa manzere ndikusiya chala chachikulu cha kumanzere, kuyambila kunja kwa zala zikhadabu za zala zala zanu mpakana ku zigongono za kumanja. Kenako pukutrani ndi manja akumanzere kuchokera nkati mwa nkono wanu mpakana nzigongono mpakana ku manja ndipo menyetsaniso mkati mwa dzanja lanu la kumanzere mosamala. Pomaliza gwiritsani ntchito chala chachikulu chakumanzere ndikupukutila kumbuyo kwa chala chaku manja. Ndipo kenako nkono wa ku manzere upukutidwe chimodzimidzi ndi wa kumanja.

Ndipo ngati mwazipukuta manja anu onse kuphatikizirapo zala zanu zonse mpakana mwakumanilana, Tayammamu yanu izakhala yololeredwa ngakhale mwayendesa kuchokera ku zala zanu za mmanja mpakana mzigonono. Komabe izi zisiyanabe ndi sunnah. Tayammamu siyoyenera kupanga muntu ndi mapazi. (mabuku oziwika bwino a khomo la chisilamu)

## **Njira makumo awiri ndi zisanu za madani pokhuzana ndi Tayammamu**

1. Zinthu zomwe zimabwera phulusa kapena kusungunuka kapena kufewa zika otchedwa zili mugulu la zilengedwe zomwe mungagwiritse ntchito tayammamu.
2. Tayammamu imaloledwa pogwiritsa ntchito nchenga, miyala ya layimu, zipangizo zotchedwa safa, ma eradi, ndi miyala ya gems, posatengela kupezeka kwa fumbi mwa zinthuzi. *(Al-Bahr-urRaaiq, Vol-1, P256)*
3. Mungagwiritse ntchito ma phale omwe apangidwa kuchokera njera zootcha, miyala yowala kwambiri kapena michenga imene. Komabe tayammamu siyololedwa ngati mupangila ndi zinthu zomwe sizili zokhuzana ndi za dziko, monga ngati Magalasi
4. Fumbi, miyala ndi zina zotero zinkhale za ukhondo zisakhale ndi tizudutswa Tina to nyasa nkati mwake, ndipo zomwe

zingapangise zinthuzo kukhala za ukhondo chokamo, mwina chifukwa cha mphepo, musagwiritsile ntchito Tayammamu sizololedwa. (*Durr-e-Mukhtar, Rad-dull-Muhtar, vol-1, p. 435*) ngati nthaka, khoma, kapena matope a pa bwalo agwera dontho za nyassi, kenalo za uma nkuzachoka ndi mphepo kapena ndi kutentha kwa zuwa ndi zoleredwa ku pemphjera (Salah) koma simungapangile Tayammamu.

5. Koma ngati mukuganizira kuti sizili za ukhondo, ndi zopanda ntchito musagwiritse ntchito.
6. Kantengo, nsalu kapena choyala pansu chilichonse (monga mphasa) ndi zina zotero, zingagwiritsidwe ntchito ndi Tayammamu ngati zili ndi fumbi lokwanila ku menesapo chala. (*Fatawa-e-‘Alamgiri, vol1, p27*)
7. Mukhoza kugwiritsa ntchito popanga Tayammamu zinthu monga izi layimu wabwino yemwe wa loredwa, matope, khoma lanjerwa la nzikiti bolani lisakhale ndi mafuta a penti, zotsalira zina ndi zina, mapepala akhoma kepena zonse zomwe zisali za chilengedwe. Ngati mabo inayikidwa pa khoma ndilololedwa kupanga Tayammamu.
8. Ngati wudhu alibe ndipo sanasambe chifukwa chosowa madzi, achite tayammamu mmalo mwake. (*Fatawa-e-Qadir-Khani with Alamgir, Vol-1p53*)
9. Ngati muli ndi mantha kuti kusamba kapena wudhu ukuwonjezerani matenda, kapena mumaziwa kuyambila kale

kuti pomwe mwasamba, kapena kuchita wudhu kudwala kukula, kapena nsilamu wina aliyense wabwinobwino koma yemwe sasata malamulo achipembezo ndi po akuziwa kuti madzi akhoza kuyambitsa utenda kwa munthuyo, akuyenera kuchita Tayammamu. (*Durr-e-Mukhtar,Rad-Dul-Muhtar,Vol-1,p441*)

10. Ngati kusamba kochokera kumutu kukuyambitsa mavuto, tsambani kuchokera mkhosi, ndipo mmutumo mungopukutamo. (*Bahar-Sharia'at, part.2, p.60*) *Madina-tu-Murshid, Bereilly Sharif*)
11. Mungachite tayammamu ngati madzi atalikira mwa mulingo wa 1 miyilosi. (*Durr-e-Mukhtar,Rad-Dul-Muhtar,Vol-1, p441*)
12. Ngati madzi a zam zam akukwanila kupangira wudhu basi ndiye kuti simungachite Tayammamu. (*Bahar-Sharia'at,part 2, p61* *Madina-tu-Murshid,Bereilly Sharif*)
13. Mungachite Tayammamu ngati mwina kusamba kukhoza kuyambitsa imfa, kapena matenda chifukwa chozizira kwambiri, ndipo kuti kulibe njira ina iliyonse ingakutetezereni kozizira. (*Fatawa-e-Alamgiri,vol-1,P28*)
14. Ngati nkayidi sakuloredwa kuchita wudhu, achite Tayammamu ndikupemphera salah yake, koma azayibwerezanso salayo kanthawi kena. Ngati ayini ndende, kapena adani ake akumuletsa kupemphera salah. a pemphere cha mumtima koma aziyibwerezanso salayo. (*bib*)

15. Munthu akagona mumzikiti ndipo mkuzilotera, amayenera asambe mokakamizidwa, ndipo akuyenela kuchoka pa mzikiti ndi kukachita Tayammamu mwanthawi yomweyo chifukwa kuchedwa ndi Haramu. Iyi ndi njira yokhayo yabwino. (Kuchokera ku Fatawa Razaviyyah, vol-3,P 492 Raza foundation Lahore). (*Fatawa –e- Alamgiri,vol-1,P28*)
16. Ngati nthawi ya pemphero (Salah) ndiyochepe, ndipo kusamba ndi wudhu zikhala za patali, muchite Tayammamu, ndipo mudzabwenzenso pemphererolo koma mutasamba mkuchita wudhu bwinobwino. (*Fatawa-e-Razaviyyah,vol-3P307*)
17. Ngati mayi wamaliza matenda amagazi oza pambuyo pochila, kapena wa maliza matenda akumwezi, ndiye madzi atalikira, akuyenera kupanga Tayammamu. (*Bahar-e-Shariat, part2, p64, Madinatul-Mushird, Bereilly Sharif*)
18. Ngati munthu ali mpa malo oti palibe china chilichonse chokwanilitsa Tayammamu, iye akuyenera ku pemphera salayo koma asachite Niyah ina iliyonse, ndipo zinthu zoyenera Tayammamu zikapezeka akuyenera kuza pempheranso swalayo koma atayika niya yake. (*Kusimikiza*) (*Bahar'-e- Shariat, Part 2, P.65*)
19. Njira ya tayammamu ndi chimodzimodzi ndi ya wudhu, kapena posamba. (*inid, P65*)

20. Ngati munthu wina sanasambe asapange Tayammamu wa wdhu ndi kusamba; mmalo mwake achite Niya ya zonsezi, koma ngati wachita ya wudhu yokha kapena kusamba kokha, ndizokwaniranso. (*Fatawa-e-Tatarkhaniyya, Vol-1, P249, Idaratul-Quran*)
21. Machitidwe omwe angapangise kuti Tayammamu ikhale yolondola, omweyo ndi amenenso alongosola kusamba kwathu ndi wudhu wathu. ndipo madzi akapezeka Tayammamu yathu idzakhalanso chimodzimodzi
22. Ngati nzimayi akuvala zozikongoletsa chitsanzo ndolo, akuyenera kuyichotsa kaye chifukwa mkutheka mbari ina ya ndolo dzanja otsafikapo munthawi ya tayammamu. (*Bahar-e-Shar'at, part 2,P.66*)
23. Mbali ya mulomo omwe umakhala mkati munthu nakatseka kukamwa upukutidwensho ndi daznja la tayammamu ngati wina atseka milomo molimba kutero kuti mbali ina ya milomo dzanja silikufikila nthawi ya Tayammamu, ndiye kuti Tayammamuyo sikhala yovomerezeka, chimodzimodzi lamulori likugwiranso ntchito nthawi ya kutseka maso molimbika. (*Bahar-e-atPart2 P66*)
24. Ngati wina akuvala mphete kapena wotch, zikuyenera zivulidwe kaye. (*Maraqil falah ma'Hashiyatu-Tahtawi, P120*) atsikana achisilamu akuyenera kuchotsa zozikolekera zonse ndicholinga choti apukute bwinobwino thupi lonse munthawi y a

Tayammamu. Pakufunika kusamala kwambili pochita Tayammamu pofanizira ndi wudhu.

25. Ngati munthu odwala kapena olumala yemwe alibe manja kapena miyendo ndipo sangapange Tayammamu yekha wina akuyenera kumuthandiza, komano Niya yake azapanga yekha munthu osati yemwe akumuthandizayo. (*Alamgiri, vol-1p26*)

## **Maganizo a madani**

Werengani bukuli ‘njira ya wudhu, ndi ya mapephero (salah) izakghala yophunzilira mmalamulo okhuzana ndi wudhu ndi sala yomwe mwandondomeko.

O Allah (عَزَّوَجَلَّ) tipangeni ife kuwerenga ndi kunva ndi kulongosoleranso anzthu malamulo osambila ndipo tipangeni kukhala osata malamulo a sunnah posamba. Amini!

Nmyamata wachisilamu wina akuti. ndi nalozedwa, usiku wina uliwonse ndi manvera nyimbo ziwiri zitatu ndi sanagone, Usiku ndimakonda kusewera Juga ndi kumapanga machismoso. Ndimakonda kukangana ndi akwathu pa zinthu zotsadziwika bwino, banja langa lidayamba kundithamangisa mnyumba kuyambira pompo chifukwa chakhalidwe langa. ndimatha kukhala ndili kunja masiku atatu kapena awiri, kenako zinthu zikakhala bwino ndimatha kubwerela mwachidule moyo wanga udali woonongeka kwambiri. Khazeni wanga Adiri Nigran wochokera kudera la Mushawarat ya Dawat-e-Islam. Adapanga



mphanvu ndi kuchita itikafu masiku khumi akumapeto kwa mwezi wa Ramadhan (1425A.H.2004) Munzikiti wotchedwa” **Adday Wali** “(Muzaffa-Gafar). Ndinali munthu osangalala ndi chikhalidwechi chomwe ndi cha Muballigh kuchokera ku Bab-ul-Madina Karachi. Ndinalapa machimo anga a mbuyo ndipo kenako ndi navala nduwila ya green yokongola yomwe adandimanga iyeyu.

Mu utsiku wa pa 27<sup>th</sup> mtima wanga wunali okhuzika kwambiri ndi duwa yomwe inachitika pakutha pa sunna. unali ulaliki wozizwa kambiri, unandipangisa ine kulira usiku onse. musiku wa chiwiri wa Eid, munthawi ya ya Fajir, ndili ntulo ndi nalota munthu wa Mulungu angundiitana dzina langa ndipo nkumatinso, ndi nthawi ya Fajir koma ukadali ntulo, munthawi yomweyo ndidapinda manja anga ngati ndikupemphera ndipo ndinazuka manja akadali chipindire momwemo.

Ndinali okhuzika kwambiri ndi maloto amenewa ndipo sindinachedwe koma kuthamangira ku nzikiti kukapemphera Fajir ndipo ndinakakhala nawo pa Ijtma ya sabata yomwe imachitika ntauni mwathu. Muchifundo cha Mulungu Allah (عَزَّوَجَلَّ), pano ndikupanga Darse-e-Nizami ku Jami’a-tul-Madina (Bab-ul-Madina Karachi). Ndine munthu wa udindo ku *Madan In’amat* mu kalasi mwanga, kunena za chisangalalo changa, ndikufuna kunena kuti Allah (عَزَّوَجَلَّ) kuti wandidalisa chifukwa ndakwanisa kuchita Madani In’amat yomwe idapangidwa ndi ophunzira. Ndi pemho langa kwa a Madani kuti abale nonse andichitile maduwa chifukwa cha kusinthika kwanga.

